Koma sakanangopempha m'njira iliyonse.

3. Kodi akanayenera kupempha m'dzina la ndani? __________

==============================================================

Tingathe kubwera kwa Mulungu kupyolera mwa Yesu yekha. M'Chipangano Chakale kuti anthu apemphere kwa Mulungu, anali kubwera ndi zopereka zawo. Iwo amapereka zopereka izi chifukwa cha machimo awo amene anali kuŵalekanitsa iwo ndi Mulungu. Tchimo lili kuletsabe kuti anthu asamalankhule ndi Mulungu. Koma ngati tilandira Yesu adzatichotsera machimo athu. Tingathe kubwera kwa Mulungu kupyolera mwa Iye.

4. Kodi Yesu anati tizipemphera bwanji? ________________

__________________________________________________

==============================================================

Palinso chifukwa china chimene ife tiyenera kupempherera m'dzina la Yesu. Kupemphera m'dzina la Yesu sikutanthauza kuti tizingonena chilichonse chimene ife tikufuna, ndipo pomaliza pake nkumangoti "M'dzina la Yesu." Ngati tipempheradi m'dzina la Yesu, ndiye kuti tiyenera kusamala kuti tizinena zinthu zimene zili zomukondweretsa. Tidzapempha zinthu zokhazokha zimene tidziŵa kuti ndizo zimene Iye amafuna kuti tikhale nazo. Tidzangopempha molingana ndi chifuniro chake.

5. Kodi tizipempha zinthu m'dzina la Yesu chifukwa chakuti tizikondweretsedwa nazo?

__________________

==============================================================

6. Kodi kupemphera m'dzina la Yesu kumatithandiza m'njira ziŵiri zotani?

__________________________________________________

__________________________________________________

Taphunzira zinthu zisanu za mmene tingathere kupemphera.

(1) Kupemphera ndi mtima onse.
(2) Kupemphera pomvera Mulungu ndi kuchita zimene amanena.
(3) Kupemphera ndi kutaya kunja maganizo ena onse.
(4) Kupemphera kosalekeza.
(5) Kupemphera m'dzina la Yesu.

7. Ziphimbeni zinthu zimenezi ndipo muyese kutchula pamtima

*************************************************************

MAYANKHO.

4. M'dzina lake.
3. M'dzina la Yesu.
6. Kumatithandiza kupeza njira yolunjika kwa Mulungu, ndipo kumatithandizanso kuti tizikhala osamala popempha zinthu zimene Iye akufuna.
2. Ayenera kupempha chilichonse chimene amasoŵa.
7. Khalani okonzeka kuzinena zimenezi mkalasi.
1. Pitirizanibe kupemphera.
5. Ayi.

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KODI CHIMALEPHERETSA MAPEMPHERO KUYANKHIDWA NDI CHIYANI?

Kuchokera ku zimene tinaphunzira sabata yatha. Tikudziŵa kuti kupemphera sichinthu chapafupi ayi. Ndipo sichinthu chakuti tingachichite monga mmene tingafunire ayi. Tinaphunzira kuti kupemphera kuyenera kuchitika m'njira zosankhidwa ndi Mulungu.

1. Lembani njira zisanu za mmene tizipempherera?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

(3) ______________________________

(4) ______________________________

(5) ______________________________

==========================================================

Koma nthawi zina ngakhale timayesa kuchita zinthu zonsezi, ndikupemphera m'njira yomwe Mulungu amafunira, komabe mapemphero athu sayankhidwa. Kodi m'chifukwa chiyani? Mwina mwake inu munali odwala ndipo munampempha Mulungu kuti akuchiritseni koma simunachire.

2. Kodi munayamba mwayesedwa kukhala ndi maganizo akuti Mulungu sayankha mapemphero?

______________________________

==========================================================

Koma Buku Lopatulika limatiuza kuti Mulungu amasunga lonjezo lake nthaŵi zonse. Buku Lopatulika limati Iye sasintha. Chabwino, nanga ndi chifukwa chiyani mapemphero athu sayankhidwa nthaŵi zina? Izi ndi zimene tikufuna kuti tiphunzire sabata ino. Buku Lopatulika limatipatsa zifukwa za kusayankhidwa kwa mapemphero athu nthaŵi zina.

Maslmo 66:18:

Ndikadasekera zopanda pake mumtima mwanga, Ambuye Ambuye sakadandimvera.

3. M'ndime iyi, kodi chimene chili kuletsa Mulungu kuti asamve mapemphero athu ndi chiyani?

______________________

==========================================================

Yesaya 59:1-2:

Taonani, mkono wa Yehova sufupika, kuti sungathe kupulumutsa; khutu lake silili logontha, kuti silingamve; koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo machimo anu abisa nkhope yake kwa inu, kuti Iye sakumva.

4. Kodi ndi chifukwa cha Mulungu ngati mapemphero athu sayankhidwa?

______________________

==========================================================

Miyambo 15:8:

Nsembe ya oipa inyansa Yehova; koma pemphero la oongoka mtima limkondweretsa.

5. Kodi ndi munthu wotani amene amamkondweretsa Mulungu ndi mapemphero ake?

______________________

______________________

==========================================================

Pa ndime zonsezi tikuona kuti sizithandiza kumpempha zinthu Mulungu pamene m'mitima mwathu muli tchimo. Mulungu safunanso kulandira zopereka zathu ngati tili ochimwa, ndiponso ngati tikukana kuvomereza machimo athu. Kodi ichi chimatanthauza machimo otani? Ife tonse timadziŵa machimo amene anthu ambiri amaŵaganiza monga bodza, kuba, ndi kupha. Ife timadziŵa kuti Mulungu sadzamvera mapemphero athu ngati tibisa osaulula zimenezi. Buku Lopatulika limanena za machimo

ena amene amaletsa Mulungu kuti atimvere. Werengani ndime iyi ndipo mupeze chinthu chimene chimatsekereza pemphero kuyankhidwa.

1 Petro 3:7:

Momwemonso amuna inu, khalani nawo monga mwa chidziwitso, ndi kuchitira mkazi ulemu, monga chotengera chochepa mphamvu, monganso wolowa nyumba pamodzi wa chisomo cha moyo, kuti mapemphero anu angaletsedwe.

6. Kodi pa ndime imeneyi, chinthu chimene chingathe kutsekereza pemphero ndi chiyani?

________________

================================================================

Inde, njira yoipa imene mwamuna amamzunzira mkazi wake imatsekereza mapemphero ake kuti asayankhidwe. Nthaŵi zina timamva anthu amene amanena zinthu zazikuluzikulu zokhudza pemphero, koma tikaona mmene amayankhulira kwa akazi awo, timadziŵa kuti Mulungu saŵamvera konse.

7. Kodi makhalidwe athu apabanja ali ofunika kwa Mulungu?

________________

================================================================

Choncho ngati mapemphero athu sayankhidwa mwaina mwake ndi chifukwa cha mmene timakhalira. Pamene tipemphera, tiyenera kuganizira miyoyo yathu ndipo timupemphe Mulungu kuti atisonyeze ngati pali chinthu china chake chimene chili cholakwika. Mwina mwake sitisamala tikamalankhula ndi anthu ena. Kapena timafuna zinthu zambiri za ife tokha. Kapena sitigwirira ntchito Mulungu monga mmene amafunira. Zinthu izi ndi machimonso.

8. Talembani mitundu ina ya machimo imene muganiza kuti ingathe kutsekereza mapemphero athu.

________________

________________

Zinthu izi zingaokeke ngati zazing'ono, koma zimatsekerezabe mapemphero athu kuti asayankhidwe. Mulungu adzatilangiza ngati titampempha. Kotero ndi chithandizo chake tikhoza kuzichotsa m'miyoyo mwathu.

9. Kodi lero taphunzira chiyani chimene chimalepheretsa mapemphero athu kuti asayankhidwe? ______________________

______________________________________________

=====================================================

*******************************************************

MAYANKHO.

3. Maganizo oipa.
4. Ayi.
1. Bwererani ku Sabata la 5 Tsiku la 5, kuti mupeze mayankho ake.
6. Pamene mwamuna samsamala mkazi wake m'njira yoyenera.
9. Tchimo, kapena mmene timakhalira.
2. Yankhani monga mmene mungaganizire.
5. Munthu wabwino.
8. Tidzazikambira mkalasi zimenezi.
7. Inde, ndi wofunika kwambiri.

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KODI CHIMALEPHERETSA MAPEMPHERO KUYANKHIDWA NDI CHIYANI?

TSIKU LACHIŴIRI:

Dzulo tinaphunzira kuti tchimo limene lili mumtima mwathu limatsekereza Mulungu kuti asatimvere mapemphero athu. Ngakhale kusamvera kwapang'ono chabe ndi tchimo ndipo kumatsekereza njira, kuti Mulungu asayankhe mapemphero athu. M'Buku Lopatulika muli tchimo limodzi limene lakhala lili kukambidwa kaŵirikaŵiri kuti ndilo limatsekereza mapemphero athu. Yesu ananena za izi pamene anali kuphunzitsa ophunzira ake kupemphera.

Marko 11:24-25:

Chifukwa chake ndinena ndi inu, zinthu zilizonse mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupiririrani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo. Ndipo pamene muimirira ndi kupemphera, khululukirani, ngati munthu wakulakwirani kanthu; kuti Atate wanunso ali Kumwamba akhululukire inu zolakwa zanu.

Mateyu 6:14-15:

Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zawo adzakhululukira inunso Atate wanu wa Kumwamba. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zawo Atate wanunso sadzakhululukira zolakwa zanu.

1. Kodi chimachitika nchiyani ngati ife sitikhululukira anthu otichimwira?

_______________________________________

=============================================================

Koma nkovuta kukhululukira. Nthaŵi zina anthu amatichitara zinthu zoipitsitsa kwambiri. Zinthu zimenezi zimasoŵetsa mtendere. Ndipo zimatipatsa madandaulo kapena kuti ululu woŵaŵa. Kodi tingozikhululukira zinthu zimenezi? Izi ndi zimene Yesu ananena. Ganizirani zimene anauza Petro.

Mateyu 18:21-22:

Pamenepo Petro anadza, nati kwa Iye, Ambuye, mbale

wanga adzandilakwira kangati, ndipo ine ndidzamkhululukira iye? Kufikira kasanu ndi kaŵiri kodi? Yesu ananena kwa iye, Sindinena kwa iwe kufikira kasanu ndi kaŵiri, koma kufikira makumi asanu ndi aŵiri kubwerezedwa kasanu ndi kaŵiri.

2. Ngati anthu apitirizabe kutichimwira, kodi tingathe kuleka kuwakhululukira patangopita kanthaŵi pang'ono chabe?

_______________

==========================================================

Ngati tileka kukhululukira abale athu ndiye kuti tili kuchimwa kwambiri ndiponso Mulungu sangamve mapemphero athu. Nanga tichite chiyani? Yesu anati, "Pamene muimilira ndi kupemphera ...khululukirani." Tingathe kupempherera chilichonse chimene tingachifune, koma pamene tili kupemphera tiyenera kumakhululukira. Ichi sichinthu chophweka kuchichita ayi. Nthaŵi zina sitingathe kukhululukira ndi mphamvu zathu zokha. Pamene tili kupemphera, tingathe kupempha chithandizo cha Mulungu, ndipo Iye adzatithandiza kuti tizikhululukira.

3. Pamene anthu ena atichimwira, kodi tiyenera kuchita chiyani ngati tikufuna kuti mapemphero athu ayankhidwe?

_______________

==========================================================

Ngakhale kusakonda anthu ena kungalepheretse mapemphero athu kuti ayankhidwe.

1 Yohane 4:20:

Munthu akati, kuti, Ndikonda Mulungu, nadana naye mbale wake ali wabodza: pakuti iye wosakonda mbale wake amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene anamuona.

4. Kodi Mulungu angamve pemphero la munthu wabodzayu?

_______________

Kodi iye angamve pemphero la munthu wadana ndi mbale wakeyu?

______________________________

==================================================

Zinthu izi zimapita mozama kwambiri. Nthaŵi zina tingaganize kuti takhulukira, pamene tikanali ndi maganizo oipa pakati pa ife ndi munthu wina wake. Nanga tiyenera kuchita chiyani?

Mateyu 5:23-24:

> Chifukwa chake ngati ulikupereka mtulo wako pa guwa la nsembe, ndipo pomwepo ukakumbukira kuti mbale wako ali ndi kanthu pa iwe, usiye pomwepo mtulo wako kuguwako, nuchoke, nuyambe kuyanja ndi mbale wako, ndipo pamenepo idza nupereke mtulo wako.

Maganizo woipa pakati pa anthu amatsekereza mapemphero awo. Ndisanayambe kupemphera, ndiyenera kuona kuti ndili ogwirizana ndi mbale wanga. Ndisangomukhululukira, koma ndiyenera kumuthandiza ngati iye ali ndi maganizo woipa ndi ine.

5. Ngati ndikhalabe wokwiya ndi ng'ombe za mnansi wanga zimene zinakadya m'munda mwanga, kodi Mulungu adzamva mapemphero anga?

______________________________

6. Kodi Mulungu adzamva mapemphero anga ngati ng'ombe zanga zinaloŵa m'munda mwa mnansi wanga, ndipo nkhaniyi sitinailongosole bwinobwino?

______________________________

7. Kuchokera m'phunziroli, kodi tchimo limene limamuletsa Mulungu kuti ayankhe mapemphero athu ndi liti?

______________________________

==================================================

************************************************************

MAYANKHO.

6. Ayi.
2. Ayi.
7. Tchimo losakhululukira, kapena kusunga udani ndi anthu ena.
3. Tiyenera kuwakhululukira.
5. Ayi.
1. Mulungu sadzatikhululukira machimo athu.
4. Ayi. Ayi.

SABATA ŁACHISANU NDI CHIMODZI: KODI CHIMALEPHERETSA MAPEMPHERO KUYANKHIDWA NDI CHIYANI?

TSIKU LACHITATU:

Taona chinthu chachikulu kwambiri chimene chimapangitsa mapemphero athu kuti asamveke kwa Mulungu. Tchimo limene lili mumtima mwathu ndilo limene limatseka njira yakuti mapemphero athu ayankhidwe.

1. M'phunziro lathu ladzulo, kodi tinati tchimo limene limapangitsa Mulungu kuti asatimvere ndi lotani?

   ___________________________________________________

==================================================

Chinthu china chimene chimatsekereza mapemphero athu ndicho kupempha zinthu zopanda pake. Tikukumbukira kuti Yesu anati tingathe kupempha chinthu chilichonse ndipo chidzachitika. Koma timaiŵala kuti anati izi zingatheke pokhapokha ngati titakhala tili wogwirizana naye.

Yohane 15:7:

> Ngati mukhala mwa Ine, ndi mawu anga akhala mwa inu, pemphani chimene chilichonse muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu.

2. Ngati ine ndikhaladi mwa Yesu ndipo mawu ake nakhalanso mwa ine, kodi ndidzafuna kokha zinthu zondikondweretsa?

   ____________________

==================================================

Koma nthaŵi zambiri timakhala tokha. Timakhalanso modzikonda. Timafuna kumadzikondweretsa. Timafuna kuti tisamasoŵe kanthu. Mwa ichi timapempherera zinthu zambiri.

Yakobo 4:2b-3:

> Mulibe kanthu, chifukwa simupempha. Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukachimwaze pochita zikhumbitso zanu.

3. Ngati ndipempha ndalama kuti ndisamasowe kanthu, kodi Mulungu adzamva pemphero langa?

________________

===========================================================

Ngati zina zifukwa zake ndi zakuti timafuna zinthu zimene zingathe kutsekereza Mulungu kuyankha ngakhale ndi mapemphero abwino omwe. Tiyeni tinene kuti mayi wina ali kupempherera mwamuna wake amene sali Mkhristu kuti atembenuke mtima. Ichi ndi chinthu chabwino, sichoncho? Inde, nanga ndi chifukwa chiyani maiyu akupempherera mwamuna wake? Kodi ndi chifukwa chakuti iye akufuna kuti adzakhale ndi umoyo wabwino pamene mwamuna wake adzakhale Mkhristu? Ili ndi funso lolimba ndithu. Zoonadi iye amafuna kuti azigwirizana ndi mwamuna wake ndi kumapempherera naye pamodzi. Kodi zidzakhala bwanji ngati Mulungu atamuitana mwamuna uja ndi kumtuma kuti akalalikire kutali ndi kwawo? Mwina mwake mayi uja adzakhala ali kukhala yekha pa nyumba kwa masiku ambiri. Kapena mwina mwake adzapita ndi kukakhala pamalo ovuta kwambiri. Mwina mwake Mulungu adzamfunsa mwamuna wake uja kuti apereke ndalama zambiri kumpingo kenaka iye naona kuti alibe ndalama zokwanira zakuti agulire zinthu. Kodi mayi ameneyu adzakondwera nazo zimenezi pamene iye ali kumpempherera mwamuna wake kuti atembenuke mtima? Pamene ife tipemphera tiyenera kudzifunsa tokha kuti, "Kodi ine ndimafunitsitsadi kuti Mulungu azikhala wokondwa, kapena ndimafuna kuti ndizikhala wokondwa ndekha?

4. Ngati ndipemphera modzikondweretsa ndekha, kodi chimachitika ndi chiyani kumapemphero anga?

________________

________________________________________________

===========================================================

Nthaŵi zina sitidziŵa kuti mapemphero athu ndi odzikonda. Timayamba kupempherera china chake chimene tiganiza kuti ndi chinthu chabwino kwambiri. Tikamapemphera, Mulungu amatisonyeza kuti chinthu ichi sichaulemerero wake. M'njira ina tikhoza kunena kuti ili ndi yankho la Mulungu. Pakali pano iye akunena kuti, "Ayi."

5. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu amapereka yankho lakuti, "Ayi" kumapemphero athu nthaŵi zina?

________________

________________________________________________________

===========================================================

Mose anali munthu wamkulu wa mapemphero. Iye anapeza mayankho kumapemphero ake. Mose anakhala wokwiya pemene anthu analilira madzi kwa iye. Iye anamunyoza Mulungu pomenya thanthwe kuti apeze madzi, m'malo mwakuti akanangonena kwa thanthwelo monga mmene anauzidwira ndi Mulungu. Pamenepo Mulungu anati chifukwa chakuti Mose anatero, iye sadzaloŵa m'dziko la Kanani. Tsopano ndifuna kuti muwerenge Buku Lopatulika ndipo mumve zimene zinachitika. Tsekulani Buku Lopatulika ku Deuteronomo mutu 3, ndime 23 mpaka 26.

6. Kodi Mulungu anachita chiyani pamene Mose anapemphera kuti apite m'dziko la Kenani?

____________________________

________________________________________________________

===========================================================

Taonani pa ndime 26 kuti Mulungu anakana pemphero la Mose chifukwa cha anthu. Mose anali m'tsogoleri. Iye ananyoza Mulungu. Anthu anayenera kuphunzira phunziro lakuti pamene tinyoza Mulungu tilangidwa. Mulungu sakanapatsidwa ulemu ngati Mose akanaloŵa m'dziko la Kanani, choncho Mulungu analikana pemphero la Mose. Anamuuzanso kuti asadzabwerezenso kupemphera pemphero lotero.

7. Pamene tiona kuti chimene tili kupempherera m'chosagwirizana ndi zofuna za Mulungu, kodi tizipitirizabe kumachipempha chinthucho?

__________________

===========================================================

Paulo analinso munthu amene anali kupemphera kwambiri. Timawerenga kaŵirikaŵiri m'makalata ake kuti anali kupempherera Akhristu kulikonse kumene anali. Nthaŵi ina Paulo

nali ndi mavuto. Iye anati m'thupi mwake munali kumuŵaŵa. Sitidziŵa kuti ichi chinali chiyani, koma tidziŵa kuti chinali china chake chimene chinali kumuvuta Paulo. Ndifuna kuti muwerenge m'Buku Lopatulika, zimene zinachitika. Tsekulani Buku Lopatulika pa 2 Akorinto mutu 12 ndipo muwerenge ndime 7 mpaka 9.

8. Kodi Paulo anapempha kangati kwa Mulungu kuti amuchotsere vuto lake?

________________________

==================================================

Mulungu anati, "Ayi, sindidzachotsa vuto limeneli. Ine ndidzakupatsa mphamvu ya kupirira. Udzaiona mphamvu yanga chifukwa chakufooka kumene uli nako pamene uli ndi mavuto aŵa."

9. Kodi Mulungu anampatsa Paulo chimene anapempha?

______________________

Kodi anamuyankha? _________________

==================================================

Yesu anatiphunzitsa kwambiri za mapemphero, kuposa munthu wina aliyense. Iye anatiuza mmene tingapempherere ndipo anatilangizanso njira yake yopempherera. Kodi tingathe kuphunzira chinthu chilichonse kuchokera ku moyo wake za mmene mapemphero athu sayankhidwira m'njira yomwe tifunira ife? Kumbukirani mmene kunakhalira usiku uja. Yesu Yesu asanapachikidwe. Iye anatenga ophunzira ake kupita nawo kumunda wa Getsemane. Kumeneko Iye anapemphera ali ndi ululu kwambiri. Tiyeni tiwerenge kuchokera m'Buku Lopatulika zimene zinachitika. Tatsekulani Buku Lopatulika pa Mateyu 26 ndipo muwerenge ndime 36 mpaka 44.

10. Kodi pamene Yesu anati, "Chilekeni chikho ichi chindipitirire," anali kutanthauza chiyani?

________________________________________

________________________________________

==============================================

Ngati Yesu akanaleka kutifera pamtanda, ndiye kuti machimo athu sakanakhululukiridwa lero lino. Kodi Mulungu anakondwa nazo zimenezi? Ayi, chikonzero chake chonse kuchokera pa chiyambi cha dziko chinali kupulumutsa anthu ku machimo awo.

11. Kodi Mulungu anavomereza pemphero la Yesu lonena kuti chikho cha imfa chimpitirire kuti asamweremo?

____________________

==============================================

Koma dziŵani, Yesu nthaŵi iliyonse anali kupempha kuti apulumutsidwe ku imfa. Iye anati, "Simonga mwa chifuniro changa koma monga mwachifuniro chanu." Yesu anafunitsitsa kuti chifuniro cha Mulungu chichitike. Ndipo ndizo zimene Mulungu anazichita.

12. Mphunziro la lero, kodi chimalephereretsa mapemphero athu kuyankhidwa ndi chiyani? ________

________________________________________

==============================================

*********************************************************

MAYANKHO.

11. Ayi.
7. Ayi.
3. Ayi.
1. Kusankhulukira.
12. Kupempherera zinthu zokonda ife tokha.
8. Katatu.
4. Mulungu sadzaŵayankha.
9. Ayi. Inde, yankho la Mulungu linali lakuti, "Ayi."
5. Chifukwa timapempha zinthu kuti tingodzikondweretsa nazo.
2. Ayi, ndidzafuna kumukondweretsa.
6. Anakana kumva pemphero la Mose.
10. Zikuoneka ngati kuti Iye anali kufuna kuti asapachikidwe.

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KODI CHIMALEPHERETSA MAPEMPHERO KUYANKHIDWA NDI CHIYANI?

TSIKU LACHINAYI:

Taona kuti mapemphero athu amatsekerezedwa ndi (1) tchimo (2) kusakhululukira, (3) kupempha zinthu modzikonda.

1. Kodi Mulungu amayankha bwanji mapemphero athu ngati tipempha zinthu zopanda pake?

_______________________________

==========================================================

Tsopano ndikufuna kuti mupeze zinthu zina zimene zimatsekereza mapemphero. Tawerengani ndime izi ndipo muone kuti ndi chiyani.

Ahebri 11:6:
Koma wopanda chikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye.

Mateyu 17:19-20:
Pamenepo ophunzira anadza kwa Yesu, ali payekha, nati, Nanga ife sitinakhoza bwanji kuchiturutsa? Ndipo Iye ananena kwa iwo, chifukwa chikhulupiriro chanu nchaching'ono: pakuti indetu ndinena kwa inu, mukakhala nacho chikhulupiriro monga kambewu ka mpiru, mudzati ndi phiri ili, senderapo umuke kuja; ndipo lidzasendera; ndipo palibe kanthu kadzakulakani kosachitika.

Yakobo 1:6-7:
Koma apemphe ndi chikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuŵinduka nayo.

2. Molingana ndi ndime izi, ngati tifuna kuti mapemphero athu ayankhidwe, kodi tiyenera kukhala ndi chiyani?

_______________________________________________

==========================================================

Mu Ahebri 11:6, tawerenga kuti sitingathe kumkondweretsa Mulungu pokhapokhapo titakhala ndi chikhulupiriro. Pamene tikubwera kwa Iye tiyenera kukhulupirira kuti Iye amayankha mapemphero.

3. Mukamapemphera nthaŵi zina, kodi mumaganiza kuti Mulungu sadzakupatsani chimene mukupempha?

   ____________________

---

Mu Mateyu 17 ophunzira anayesera kuti atulutse chiŵanda mwa mnyamata wina. Koma analephera kutero. Pambuyo pake Yesu anachitulutsa chiŵanda chija. M'ndime 19 ndi 20 zimene tawerenga pamwambapo, ophunzira anamfunsa Yesu chifukwa chiyani iwo analephera kutulutsa chiŵanda chija.

4. Taŵerenganinso ndime zimenezi ndipo mufotokoze mmene Yesu anaŵayankhira ophunzira ake aja.

   Iye anaŵayankha kuti ____________________

   ____________________

---

Kusakhulupirira ndiko kumaletsa mapemphero athu kuti asayankhidwe. Yesu ndiye ananena zimenezi. M'Buku Lopatulika pa Yakobo, zomwezi zinanenedwanso. Taŵerenganinso Yakobo 1:6-7:

5. Kodi munthu wokayika m'chikhulupiriro chake amalandira chiyani akamapemphera?

   ____________________

---

Koma ichi sichachilendo kwa ife. Timadziŵa kuti tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro tikamapemphera. Koma nthaŵi zina sitikhala ndi chikhulupiriro ndipo sitidziŵa chochita. Kodi tikhoza kukhala nacho bwanji chikhulupiriro? Sabata ya mawa tidzatha nthaŵi tikuphunzira zimenezi.

6. Mu phunziro limeneli, kodi chimene chimatsekereza mapemphero athu ndi chiyani?

______________________________

7. Nanga zina zolepheretsa mapemphero ndi ziti?

(1) ____________________ (2) ________________________

(3) ____________________________

============================================================

************************************************************

MAYANKHO.

4. "Chikhulupiriro chanu ndi chaching'ono."
6. Kusakhulupirira.
1. Iye amayankha kuti Ayi.
3. Inu ndinu amene mungathe kuyankha funso ili.
5. Salandira kanthu.
2. Tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro.
7. (1) Tchimo, (2) Kudzikonda, (3) Kupempha zinthu modzikonda.

SABATA LACHISANI NDI CHIMODZI: KODI CHIMALEPHERETSA MAPEMPHERO KUYANKHIDWA NDI CHIYANI?

TSIKU LACHISANU:

Ndiganiza kuti sitiri odabwa poona kuti mapemphero athu ambiri sayankhidwa. Taonanso zinthu zambiri zimene zimatsekereza mapemphero athu. Kodi mungazikumbukire?

1. Ngati mufuna mungathe kuonanso zimene mwaphunzira pamasiku anayi apitawo. Tsopano lembani zimene zimatsekereza mapemphero pano.

   (1) ____________________ (2) ____________________

   (3) ____________________ (4) ____________________

==========================================================

Pamene tinali kuphunzira za mmene tingapempherere, tinaona kuti chinthu chimodzi mwa zinthu zofunika kwambiri ndi kupemphera kosalekeza. Nanga chimachitika ndi chiyani ngati sitipitirizabe kupemphera? Timaphunzira kuti mapemphero sayankhidwa ngati tilekeza kupemphera. Choncho, pano palinso china chimene chimatsekereza pemphero.

2. Kodi ndi chinthu chotani chatsopano chimene timaona kuti chimatsekereza pemphero?

   ______________________________

==========================================================

Ndime imodzi imene timaikonda kwambiri pa ndime za mapemphero ndi iyi yochokera pa Mateyu 7:7:

> "Pemphani ndipo mudzapatsidwa, funani ndipo mudzapeza, gogodani, ndipo mudzatseguliridwa."

M'chinenero chimene Yesu anali kugwiritsira ntchito pamene Iye anali kunena mawu amenewâ, anali kunena kuti, "Mupitirizebe kupempha; mupitirizebe kufuna, mupitirizebe kugogoda. M'ndime yotsatira Iye anati pamene titero ndiye kuti tidzalandira mayankho a mapemphero athu.